Kuti pamene tikubatiza machimo achoke, kulapa ndiko mkusiya; kodi munthu akuti ndikhalabe molakwika momwemu (banja lolakwika) koma ndalapa, kodi uyu akhoza kukhala walapadi? Tangoganizani kuti amuna okhaokha akwatirana anakali kunja kwa Mpingo ndiye tawalalikira za Mpingo afuna kukhala akhristu ndiye anene kuti tibatizidwa popeza ubatizo umachotsa machimo ndiye ngati banja lathuli linali loipa pamaso pa Mulungu tikabatizidwa popeza machimo achoka sitisiyanabe likhalabe banja ndipo likhala loyenera popeza machimo anthu achoka, kodi tikhoza kuwavomera popeza ubatizo wachotsa machimo awo? Ndikhulupilira kuti sitingavomere popeza banja lolakwika limakhalabe lolakwika ngati palibe kulapa.

Kodi mwava za momwe pachiyambi Mulungu anaikira banja? Kodi banja lanu mlolondola pamaso pa Mulungu malingana ndi chiyambi? Kodi poweluza malingana ndi Yohane 12:48 mawu a Mulungu akakuweluzani bwanji pa banja lanu? Kwa amene tili pa banja lofanana ndi chiyambi tikumbukire mawu a Solomoni pa Mlaliki 9:9

OLEMBA: VINJERO CHIVWATI GONDWE

MPINGO WA KHRISTU

P.O.BOX 2405

LILONGWE.

CALL/WHATSAPP-- 0997 847 826 / 0882 766 018

BANJA: KODI ZINALI BWANJI PACHIYAMBI?

Yesu pamene anali pa dziko lapansi, nthawi ndi nthawi Afarisi anamutsata koma cholinga chawo kwambiri amafuna kumuyesa (Mateyu 16:1,22:15-22) kuti ampeze olakwa. Buku la Mateyu 19:1-10 Afarisi monga mwa chizolowezi chawo anadza kwa Yesu kuti amuyese (v3) pokamba za banja ndipo anamufusa Yesu, "…. Kodi nkuloledwa kuti munthu achotse mkazi wake pa chifukwa chilichonse?" koma Yesu adayankha powafusanso fuso v4- "… Kodi simunawerenga kuti Iye (Mulungu) amene adalenga anthu pachiyambi, analenga iwo mwamuna ndi mkazi'' pachiyambi pomwe Yesu akunena ndipa Gesesis 2:7,22-24.

Yesu anaona kuti mkoyenera kuti anthu adziwe chiyambi cha zinthu, anazindikira kuti tikadziwa chiyambi nthawi zonse tikakumana ndi fuso kapena vuto sitikonza potengela nthawi yomwe tili, koma tidziyang'ana choyenera chomwe chiri chiyambi cha zinthu. Pachiyambi Mulungu adayika kuti zoyenera ndi Mkazi m'modzi komanso mwamuna m'modzi. Munthu akhoza kukhala ndi maganizo ake ammene afunira kuti banja likhalire, koma chofunika simaganizo anthu ayi, koma zomwe Mulungu anaika pachiyambi. Pa Mateyu 19:5-6, " v5 nati, chifukwa cha ichi mwamuna adzasiya atate wake ndi amake, nadzaphatikizana ndi mkazi wake, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi? V6 Chotero kuti salinso awiri koma thupi limodzi. Chifukwa chake ichi chimene Mulungu anachimanga pamodzi, munthu asachilekanitse".

ZINTHU ZITATU ZOMWE MULUNGU ANAIKA PACHIYAMBI CHA BANJA

Choyamba mchakuti banja limafunika likhale la mwamuna mmodzi komanso mkazi mmodzi (Mateyu 19:4). Kutathauza kuti Mulungu sanakonze kuti banja lidzikhala ndi mwamuna mmodzi ndi akazi awiri kapena kuposera pamenepo. Banja lomwe muli amuna kapena akazi okhaokha limenero ndi banja lomwe Mulungu sanaliyike pachiyambi ndipo ngati sanaike, ndiye kuti sibanja loyenera ndipo ngati sibanja loyenera mathero ake ndi kumoto (Gahena).

Chinthu chachiwiri chomwe anaika ndi chakuti pamene mwamuna wakwatira amayenera kusiya makolo ake (Mateyu 19:5). Akati kusiya makolo zimayimira kuti popeza munthu wokwatira amakhala wamkulu, ayenera kusitha kachitidwe kake ka zinthu. Popeza wakwatira ayenera iye ndi mkazi wake athe kuyambano kupanga ziganizo zomwe adziyendetsera banja lawo. Munthu ukakhala ndi makolo umayendera ziganizo za makolo ako, pomwe wakwatira makolo sayenera kukupangirani ziganizo zoyendetsera banja lanu (Akhoza kupereka malangizo osati ziganizo).

Chachitatu chomwe anaika mchakuti anthu akakwatirana amaphatikizana kukhala nthupi limodzi (Mateyu 19:5). Masamu a Mulungu amati chimodzi (Mwamuna) kuphatikizanso chimodzi (Mkazi) amapangabe chimodzi (Banja loyenera). Tidziwa kuti awa ndimasamu osiyana ndithu ndi mmene masamu adziko amayendera koma Mulungu akuti umu ndiye ziyenera kukhalira tikafika pa banja. Mpake Paulo anayakhula kuti pamene anthu akwatirana "Mkazi alibe ulamuliro wa thupi lake la iye yekha, koma mwamuna ndiye; koma momwemonso mwamuna alibe ulamuliro wa thupi la iye yekha, koma mkazi ndiye" 1 Akorinto 7:4. Anthu akakwatirana zinthu zimasitha popeza awiri amakhala thupi limodzi. Pa 1 Akorinto 7:2 akuti " Koma chifukwa cha madama munthu yense akhale naye mkazi wa iye yekha, ndi mkazi yense akhale naye mwamuna wa iye yekha" zomwe ananena Paulo apa sizikusiyana ndi zomwe Mulungu anaika pachiyambi kuti mwamuna mmodzi komanso mkazi mmodzi. Pamene Paulo ananena kuti **WA IYE YEKHA** amafuna kutathauza chani? Tikumbukire kuti Mulungu sanakonze kuti banja likhale ndi mwamuna mmodzi ndi akazi awiri ayi; pamene banja liri lakuti mwamuna ali ndi akazi awiri ndiye kuti mwamuna ameneyu sali pa banja loyenera momwemoso pomwe mkazi ali pa banja loti mwamuna ''**wawo**'' ali ndi akazi awiri, akazi amenewo onse sali pa banja lomwe tingati ali ndi mwamuna "**wa iye yekha**''.

Dziko lapansi limagwiritsa ntchito mawu akuti "**mkazi wamkulu**" (mkazi woyamba) kapena "**mkazi wang'ono**" (mkazi wachiwiri) pofuna kufotokoza za banja lomwe mwamuna yemwe ali ndi akazi awiri. Ndipo kwa anthu ambiri mkazi amene amakhala olakwa ndi mkazi wang'ono ndipo ena amati mkazi wamkulu ndiamene ali pa banja lam'malemba popeza ndi woyamba. Koma fuso labwino mlakuti kodi pamene munthu ali pa banja lotele kodi tinganene kuti ameneyo (mkazi wamkulu) ali pa banja ndi mwamuna wa iye yekha? Nanga kodi pachiyambi Mulungu anati banja loyenera limakhala ndi mkazi wa mkulu komaso wang'ono? Munthu amene ali pa banja losephana ndi chiyambi chomwe Mulungu anaika ayenera kuti achoke kuti akapeze moyo wosatha. Tikumbukile kuti banja limatha ngati wina wachita chigololo (Mateyu 19:9) kutathauza kuti ngati mkazi wamkulu mwamuna wake akakwatila mkazi wina ali omasuka kuchoka pa banja lotero popeza mwamunayo wamasula banja popanga chigololo ndipo mkaziyo akhoza kukakwatiwa ndi mwamuna wa iye yekha (mwini). Pamene Yesu ananena kuti amene akwatira ochotsedwayo naye achita chigololo kodi amafuna kutathauza chani? Kuti ziveke bwino vesi tiyidula motere v9, "Ndipo ine ndinena kwa inu, Amene aliyese akachotsa mkazi wake, kosakhala chifukwa cha chigololo……" mukumbukile kuti banja likhoza kutha ngati wina wapanga chigololo, ndiye awa omwe Yesu wanenawa achotsana osati chifukwa cha chigololo. Kodi pamene anthu achotsana popanda chigololo zimayenera kutani? Paulo anayakha izi 1 Akhorinto 7:10-11 apa ananena kuti ngati anthu asiyana pazifukwa zina osati chigololo akhoza kusiyana koma sayenera kukhalaso pa banja koma ngati afune banja adziwe kuti " ….ayanjanitsidwenso ndi mwamunayo…." V 11. Yesu amafuna kutathauza zimenezo kuti pamene anthu asiyana osati chifukwa cha chigololo "…… ndipo iye amene akwatira wochotsedwayo, achita chigololo'' koma amene atenga mkazi/mwamuna wakuti achoka ku banja lomwe latha pachifukwa cha chigololo sakupanga chigololo ngati mkaziyo / mamunayo ali okuti sanapange chigololo ndiyeyo komwe achokako.

TINALI KUNJA MPAKE ZINATELE

Awa ndi mawu omwe anthu ambiri amayakhula kuti ifetu tinasiyana ndi Akazi/Amuna athu oyamba popeza tinali kunja; tinali tisanakhale akhristu-tinali tisakudziwa lamulo la Mulungu pa nkhani ya banja. Tisaiwale kuti lamulo la banja linaperekedwa nthawi ya Adamu ndi Hava (Nthawi ya Makolo) pomwe Mpingo komanso lamulo la Mose (la Mulungu) lisanaperekedwe, Mpingo komanso lamulo la Mose linapeza lamulo la banja lilipo kale. Kutathauza kuti lamulo la banja linapita kwa munthu aliyese osati kwa mkhristu yekha. Anthu onse anakhala nthawi zitatu za Baibulo anayenera kusunga lamulo loti mkazi mmodzi kapena mwamuna mmodzi monga pachiyambi. Ena amati popeza anali kunja ndiye pano popeza afuna kukhala akhristu tikhoza kuwabatiza popeza ubatizo umachotsa machimo (Machitidwe 22:16) ndiye banja lolakwikali likhalano labwino. Zoona kuti ubatizo umachotsa machimo koma tisaiwale kuti munthu amayenera kulapa (Luka 13:3)